

# UTHENGA WABWINO WA CHOONADI


MALANGIZO NDI CHILIMBIKITSO KUCHOKERA M'BAIBULO  
KUPITA KWA AMENE AKULALIKIRA UTHENGA WABWINO

## KUGWA KWA MUNTHU WANZERU

Yehova Mulungu anati kwa Solomo, “Tapempha chimene ndikupatse,” (1 Mafumu 3:5). Mmallo mopempha chuma, kutchuka kapena moyo wautali, Solomo anapempha Yehova nati, “Patsani tsono kapolo wanu mtima womvera wakuweruza anthu anu; kuti ndizindikire pakati pa zabwino ndi zoipa...” (9). Yehova anakondwera ndi pempho la Solomo namupatsa nzeru zimene panalibe wina wolingana naye pa masiku amenewo, ngakhale mtsogolo mwake (12). Solomo anadziwika natchuka ngakhale ku maiko akutali chifukwa cha nzeru zake zakuya komanso mtima wake wakuzindikira zinthu.

Solomo analemera ndipo anadalitsidwa chifukwa cha mphatso yake ya nzeru zochokera kumwamba. Iye anamanga kachisi wokongola wopembedzeramo Yehova. Ngakhale Solomo anali ndi nzeru zochulukira chotere, iye sanamvere Mulungu nakonda akazi achikunja a maiko ena amene amapembedza mafano. Mulungu anapereka lamuo ili mwachimvekere kuti, “Inu musakalowa kwa iwo, ndipo iwo asadalowe kwa inu; zedi adzatembenusa mitima yanu kutsata milungu yao; amenewo Solomo anawaumirira kuwakonda.” (1 Mafumu 11:2).

“Ndipo kunali, atakalamba Solomo, akazi ake anapambutsa mtima wake atsate milungu ina; ndipo mtima wake



*Akazi a Solomo  
anatembenusa mtima  
wake natsatira milungu ina.*

sunakhala wangwiro ndi Yehova Mulungu wake monga mtima wa Davide atate wake.” Ndi zomvetisa chisoni kuona mmene anagwera ndi kuthera munthu wanzeru ngati Solomo.

Panthawi imeneyo, Solomo amaganiza kuti anali wochenjera pokwatira akazi a mitundu ina popeza iye amapangananso za mtendere ndi maiko amene iwo amachokerako. Iye sanalabadire malangizo a Yehova, naganiza kuti mtima wake unali wolunjika pa Yehova ndi kuti sadzachokamo mu njira ya chilungamo.

Solomo sanapambuke pamaso pa Mulungu pakamodzi. Pang’ono ndi pang’ono, iye anakopeka ndi akazi ake achikunja. Tangoganizani mmodzi mwa akazi ake akubwera kudzapempha ndalama zomangira kachisi wa mulungu wake wosema. Solomo poyamba akuyankha nati, “Ine sindikhulupirira milungu yanu yosemayo, komabe nazi ndalama.” Kenaka mkazi uja akubweranso nati, “Wokondeka a Solomo, inu a daling’i anga, kodi simungathe kubwera ku mwambo wotsekulira kachisi wokongola amene mudamangira Mulungu wanga uja.” Atakambirana kangapo ndi akazi ake amene sanapembedze Mulungu woona, pang’ono ndi pang’ono Solomo anayamba kusiya kudzudzula choipa ndipo kenaka anatheratu. Pata-pita zaka zambiri, mtima wake unatembenuka pamaso pa Mulungu mpaka potsizira anachita choipa pamaso pa Yehova.

(Zapitirira pa tsamba 2)

Mau a Mkonzi

Tsamba 3

Kusanthula Mau a  
Mulungu:  
Mphamvu za Chikoka

Tsamba 4

Nkhani yothandizira:  
Mphamvu ya Chikoka

Tsamba 5

Muyeso wa Baibulo pa  
za Mafilimu ndi TV  
Tsamba 7  
Mafunso ndi Mayankho:  
Tsamba 9

Kodi mukudziwa?

Mau a pa nyengo yake

Tsamba 10

# zimene BAIBULO limaphunzitsa za...

## Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

## Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

## Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

## Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;

Aef. 2:1, 5-6

## Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

## Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

## Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;

Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

## Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

## Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;

Akol. 1:18

## Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

## Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;

1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

## Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

## Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;

1 Akor. 7:10-11

## Chikhaliidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

## Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;

Mat. 25:31-46

## Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

## Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

## Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

Solomo anatembenuka pamaso pa Mulungu chifukwa cha kukopeka ndi akazi ake. Tiyeni tiphunzire pamene tikulingalira za nkhani iyi yomvetsa chisoni ya kugwa kwa munthu amene anali wanzeru kuposa onse. Tiyenera tichenjere ndipo tisamale ndi zinthu zimene zikukopa mitima yathu. Sitingakhale auzimu kwambiri nkusakopeka ndi zinthu zoipa ngati tidzipereka tokha ku zimenezo. Ngakhale titakhala kuti tili ndi zolinga zabwino, iwo olimbawo adzayamba kuchisisita choipa chija; ndipo moyo wao wa uzimu udzazilala ngati moyo wa chiyero sukhala chinthu chofunikira pa moyo wao. Ngakhaletu mwala waukulu umabooledwa kadzenje ngati madzi akudonthezera pamodzimidzi pomwepo kwa zaka zambiri.

Mdirekezi sasamalira kuti zitenga nthawi yaitali bwanji kuti akubereni chipulumutso chanu. Iye adzayesetsa kuzimitsa chazimu chimene chili mwainu pokukopani ndi zinthu zokoma zimene zimapezeka m'dziko lino. Anthu akusiya kudziyang'anira pa moyo wao wauzimu, ndipo akulola kuti zinthu zadziko lino zitanganidwitse moyo wawo. Chilichonse chimene mumachita, kulikonse kumene mumapita, zimene mumamvera kapena kuonera, anthu amene mumayanjana nawo ndi zina zonse zili ndi mphamvu yaikulu yokopa moyo wanu. Kumbukirani mmene anagwera ndi kuthera Solomi mu ukalamba wake. Yendani mosamala komanso m'moyo wapemphero ndipo muchenjere ndi zinthu zokuzungulirani zimene zili ndi mphamvu yokukopani ndi kuzimitsa chazimu chimene chili mwa inu.

-mws

## UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa mkalata umene umasindikizidwa m'dzina la Ambuye kwa anthu onse ku maiko onse ndi cholinga chofuna kuwakhazikitsa ndi kuwalimbikitsa mu choonadi cha Mau a Mulungu. Kalata uyu akuphunzitsa ndi kulimbikitsa zooni za Baibulo zimene zakhazikitsidwa kuyambira pa nthawi ya Khristu ndi ya atumwi.

Mau a Mulungu ndi okhawa amene ali muyeso wovomerezeka wa chikhulupiriro. Amaphunzitsa chipulumutso ndi mamasulidwe kuchokera ku uchimo kudzera mu ntchito ya maombedwe ya mwa Yesu Khristu; komanso kudzazidwa ndi Mzimu Woyera kumene kumatsatirapo. Ndipo kumatithandiza kuti titsogolere, tiwongolere ndi kuwapatsa ena mphamvu; komanso tikhale ndi chiyero choonekera pa gawo lililonse la moyo wa munthu kuphatikizapo mgwirizano ndi umodzi wa anthu a Mulungu. Utumiki wovomerezeka wa kwa Mulungu uli mu mwa anthu amene ubale wao wachikondi wazikika pa choonadi.

Akonzi: Michael & Rene Smith

## KUTI MULANDIRE NAWO KALATAYI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa kalata umene timasindikiza miyezi itatu iliyonse molingana ndi chitsogozo cha Ambuye. Kuti mulandire nawo kalatayi maulere pa [email](mailto:editor@thegospeltruth.org), pitani pa intaneti ndipo mutipeza pa [www.thegospeltruth.org](http://www.thegospeltruth.org). Muli omasuka kutitumizira maina ndi ma [email](mailto:editor@thegospeltruth.org) a anthu amene akufuna kulandira nawo kalatayi. Mainawa muwatumize kwa mkonzi.

## KUTI MUTIPEZE

Uthenga Wabwino wa Choonadi imasindikizidwa mu maiko osiyanasiyana kuti igawidwe m'maikowo. Ntchito yosindikiza kalatayi komanso mautumiki ena ochitika ndi ofesi yathu pothandiza kufalitsa uthenga wabwino amathandizidwa ndi zopereka zaufulu zoperekedwa mdzina la mpingo wa Mulungu.

The Gospel Truth, P. O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA

editor@thegospeltruth.org

# Mau a Mkonzi



*Pakuti chaonekera chisomo cha Mulungu chakupulumutsa anthu onse, ndi kutiphunzitsa ife kuti, pokana chisapembedzo ndi zilakolako za dziko lapansi, tikhale ndi moyo m'dziko lino odziletsa, ndi olungama, ndi opembedza.*

—Tito 2:11-12

Ngakhale kuti uchimo ukupezeka paliponse, Khristu anapereka zonse zoyenerera kuti tikhale m'moyo uno, mu dziko ili loipali. Pakati pa zilakolako za dziko lapansi ndi chisapembedzo, ife tikuitanidwa kukhala moyo wa chilungamo. Mtolo umene Mulungu waika pa mtima panga ulendo uno uli pa mutu wa 'chikoka.' Pali zinthu zambiri zimene zili ndi chikoka champhamvu ndipo chikokacho chimanka chikulirakulira nthawi ikamapita. Akhristu amvula zakale akhala akundiuzwa kuti masiku ano dzikoli lili ndi chikoka chambiri kusiyana ndi kale. Tikuyenera kukhala anzeru ndi kuzindikira zinthu zimene zatizungulira zomwensho zili ndi chikoka chachikulu.

Zimandimvetsa chisoni mu mtima mwanga ndikamaona akhristu ochuluka, amene amadziwika kuti ali ndi moyo wachiyero, akuchita ngati kukhala moyo wachiyero ndi nkambakamwa chabe komanso ngati 'zinthu' zosafunikira. Makolo ambiri akupatuka natsata njira ya dziko lapansi ndipo amene adzakolole ndi ana awo. Pali chifukwa chimene anthu ambiri sakukhala ndi mphamvu komanso kudzodza pa moyo wawo. Tiyenera kubwezeretsa muyeso wachiyero ndi kulimbana ndi chikoka cha uchimo.

Zikoka zosiyanasiyana zimene dziko lino liri nazo ndi zokoma m'maso ndipo pamatenga nthawi kuti tione zotsatira zake zenizeni pa miyoyo ya anthu. Ndikoyenera kuti tiwunguze ndi kuzindikira zotsatira zake za anthu amene ataya moyo wao wa chiyero. Ndikudikira ndidzaone uzimu weniweni kuchokera kwa munthu amene atsegula khomo la mtima wake ku zikoka za dziko lino. Pamene dzikoli likunka liyipyayipira, padzayenera kukhala kusiyana kwakukulu pakati pa anthu a Mulungu ndi anthu ena amene timakhala nawo. Sitiyenera kudziyesa tokha pofanizira ndi dzikoli koma ndi muyeso wa Mau a Mulungu.

Mothandizidwa ndi Mulungu, mu kalata iyi ya The Gospel Truth ndalembo mfundo zingapo zimene anthu sazimvetsetsa ndipo pamakhala kutsutsana pakati pawo. Mfundo zake ndi monga intaneti, mafilimu, TV, nyimbo ndi zina zotere. Nkofunikira kuti tisakhale kakaka kapena kudziteteza pa kaganizidwe kathu. Tiyeni mwachilungamo tiunikire mphamvu ya chikoka. Tiyeni titsekule mitima yathu ndi kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera.

Inu mwana wa Mulungu, kodi mungathe kunenadi kuti kena kalikonse pa moyo wanu ndi kolungama ndi koyera pamaso pa Mulungu? Kodi ndi zotheka kuti mwina mtima wanu unazilala pa zauzimu? Chikoka chimene dziko lapansi likufuna kutipangitsa ndi kuti ife tikhale olekerera, okhudzidwa ndi ololela ku zinthu za uchimo. Tiyeni tikhale oona ndi okhulupirika polimbana ndi zoipa za dzikoli.

Michael W. Smith

January 2014

Zambiri Zili pa  
INTANETI

*Mukafuna kutipeza  
pa intaneti, mulembe  
[www.thegospeltruth.org](http://www.thegospeltruth.org)  
kuti mudzilandira  
makalata athu  
kapenanso kuti muone  
makalata akale.*



## Zikoka Zadziko

Oyanjana nawo

Osakhulupirira

Mafilimu

TV

Zosangalatsa moyo

Nyimbo

Masewero

Za utolankhani

Malo auchimo

Chinyanso

Zilakolako

Chidetso

Ufiti

Zoledzeretsa

Mankhwala osokoneza

bongo

“SIMUDZAPERKA  
**CHIKOKA**  
KU DZIKO LAPANSI  
POFUNA  
KUKHALA NGATI  
ILOLO.”

# KALOZERA POSANTHULA MAU A MULUNGU

## MUTU: MPHAMVU YA CHIKOKA

**Mau a Mulungu:** *Chotupitsa pang'ono chitupitsa mtanda wonse.* —Agalatiya 5:9

**Chidule:** Mdaniyo akugwiritsa ntchito zikoka zambiri m'dziko lino zooneka zokoma mmaso pofuna kuwakanghira anthu kutali ndi chiyeero. Anthu a Mulungu akuyenera kuchenjera ndithu pamene komanso mmene mdierekezi akugwirira ntchito ndipo achotse zikoka zopanda umulungu pa moyo wao ndipo mmalo mwake akhale ndi zikoka zimene zili zabwino ndi zoyera.

**Tanthauzo:** Chikoka — Mphamvu kapena kuthekera yosintha kapena kupangitsa kuti chikhali-dwe, chitukuko, kapena mkhalidwe wa munthu kapena chinthu zisinthe moonekera kapena mo-saonekera, kuweyeseka.

### 1. Onse Akhoza Kukopeka

- A. Machitidwe 14:14-15 Anthu a mkhalidwe ngati wathu.
- B. Salmo 103:14 Ndife fumbi.
- C. Mateyu 26:41 Thupi ndi lofooka.
- D. Miyambo 6:27-28 Moto mu chifuwa.
- E. Mateyu 6:22-24 Simungatumikire Mulungu ndi chuma.

### 2. Zitsanzo Kuchokera mu Baibulo

- A. Genesis 3:1-8 Adamu and Heva.
- B. Oweruza 16:18-20 Samusoni.
- C. 1 Mafumu 11:4 Solomo.
- D. Luka 22:55-62 Petro.

### 3. Samalani

- A. Agalatiya 6:7-8 Udzakolola chimene wafesa.
- B. Yesaya 5:20-22 Kunena choipa kuti nchabwino.

### 4. Mphamvu ya Zinthu Zazing'ono

- A. 1 Akorinto 5:6 Chotupitsa pang'ono.
- B. Nyimbo ya Solomo 2:15 Tiankhandwe tating'ono.
- C. Mlaliki 10:1 Ntchentche zakufa.

### 5. Chikoka Cholakwika

- A. Agalatiya 5:19-21 Ntchito za thupi.
- B. 1 Akorinto 15:33 Mayanjano olakwika.
- C. 2 Akorinto 6:14-17 Osakhulupirira.
- D. Miyambo 7:7-26 Chilakolako.
- E. Aefeso 5:18 Vinyo.

### 6. Kanizani Chikoka cha Chisapembedzo

- A. Miyambo 4:14-15 Musalowe.
- B. 2 Timoteo 2:22 Thawa zilakolako zau-nyamata.
- C. Aefeso 5:6-13 Muwatsutse.
- D. Masalmo 141:4 Musamvere.
- E. Aefeso 4:27 Musampatse mpata mdierekezi.
- F. Yakobo 4:7-8 Mukanizeni mdierekezi.

### 7. Sungani Maganizo ndi Mtima

- A. Miyambo 4:23 Sunga mtima wako.
- B. Mateyu 5:29-30 Ngati diso lako liku-chimwitsa.
- C. Masalmo 101:3 Sindidzaika chilichonse choipa.
- D. Ahebri 12:13-15 Tsatani chiyeero.
- E. 1 Akorinto 6:12 Si zonse zili zopindulitsa.

### 8. Zikoka Zabwino

- A. Ahebri 10:24-25 Kusonkhana kwathu pamodzi.
- B. 1 Yohane 1:5-7 Chiyanjano.
- C. Miyambo 27:17 Chitsulo chimanola chitsulo chinzake.
- D. Masalmo 119:11 Mau a Mulungu.
- E. Masalmo 1:1-2 Wodala munthuyo.

### Mau omaliza

*Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansipano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire chimene chili chifuno cha Mulungu, chabwino, ndi chokon-dweretsa, ndi changwiro.*

—Aroma 12:2

# MPHAMVU YA CHIKOKA

*Mau othandiza pa Kusanthula Baibulo*

## MDANI WA MIYOYO ALI PA NTCHITO

Satana akuchita nkondo motsutsana ndi anthu a Mulungu. Cholinga chake ndi kufuna kuwononga gwero lenileni la uzimu wao. Pamene sitingathawe kuyesedwa, choopsa chachikulu ndicho zikoka zimene zimakakamiza ana a Mulungu kuti nkupita kwa nthawi achite kusamvera.

## ONSE AKHOZA KUKOPEKA

Chikoka ndiyo mphamvu yosintha chikhalidwe kapena mkhalidwe wa munthu wina wake. Ngati munthu akadali mu thupi lanyamali, adzayesedwa ndi mphamvu ya chikoka. Paulo ndi Barnaba ananena kuti iwo anali “anthu a mkhalidwe wathu umodzimidzi ndi wanu” (Machitidwe 14:15). Nchifukwa chake Yesu anawachenjeza ophunira ake kuti, “Chezerani ndi kupemphera, kuti mungalowe m'kuyesedwa: mzimutu uli waku-funa, koma thupi lili lolefuka.” (Mateyu 26:41). Musakhale akusadziwa za mphamvu ya zikoka zoipa. Akhristu ambiri amachita nawo zinthu zadziko ndi zinthu zosangalatsa zimene zimadetsedwa ndi dzimbiri la uchimo. Iwo amadabwa kuti ndi chifukwa chiyani sakhala m'moyo wa chipambano ndi wamphamvu mwa Mulungu. “Kodi mwamuna angatenge moto pa chifuwa chake, osatentha zovala zake?” (Miyambo 6:27).

## ZITSANZO ZOCHOKERA M'MALEMBA

Malemba ali ndi zitsanzo za anthu amphamvu amene anawa chifukwa cha mphamvu ya chikoka choipa. Pachiyambi Adamu ndi Hava anataya chiyero chawo ndi ungwiro wawo pamaso pa Mulungu chifukwa anamvera ku mau okoma koma abodza ndi chinyengo cha njoka (Genesis 3:1-8). Samusoni anachita chibwenzi ndi Delila, ndipo sichinali chofuna chake kuti awululile chinsinsi cha gwero la mphamvu zake zochulukira (Oweruza 16:18-20). Pali zikoka zosiyanasiyana pa moyo wathu zimene pang'ono ndi pang'ono zimadya mphamvu yoletsera uchimo mpaka

tikafooka, pamapeto ake timagwa mu uchimo. Solomo mu ukalamba wake anachoka pamaso pa Mulungu chifukwa cha chikoka chochokera kwa akazi ake ambiri (1 Mafumu 11:4). Petro wophunzira wa Yesu anamukana Ambuye chifukwa choopa khamu la anthu (Luka 22:55-62). Anthu ambiri apatuka pa njira ya chiyero pololera kuti zikoka za dziko lino ziwakope komanso posatha kuima njii motsutsana nazo.

## MPHAMVU YA ZINTHU ZING'ONOZING'ONO

Pali mphamvu yaikulu mu zikoka zing'ono. “Kodi simudziwa kuti chotupitsa pang'ono chitupitsa mtanda wonse?” (1 Akorinto 5:6). Kawirikawiri amakhala “ankhandwe, ngakhale ang'ono, amene akuononga minda yamipesa” (Nyimbo ya Solomo 2:15). Nthawi zonse si machimo akuluakulu amene amapangitsa kuti akhristu ataye chipulumutso chawo. Zimayamba ndi tinthu tating'ono, tokhala ndi chikoka ndipo kenaka izi zimasintha mmene munthu amaganizira komanso mmene amaonera za choonadi ndi chiyero. Mumayamba kunena kuti, “Komatu si uchimo, ndikhoza

kupita kumeneko. Ndikhoza kumvera nyimbo yakuti ija. Ndikhoza kuonera filimu imeneyo. Ndinapulumutsidwa ndipo sindichita chilichonse cholakwika.” Anthu amene amanena mau ngati amenewo pambuyo pake amagwa mu uzimu wao. Ganizirani za chikoka chimene chili mu zinthu ngati zimenezi. Kodi moyo wanu wauzimu umakhudzidwa bwanji? Kodi mumaona kukakamizidwa kuchita zinthu zimene sizili zolondola? Kodi m'aganizo anu mukuwadyetsa ndi zinthu zimene sizili zoyera ndi zolungama. Khalani anzeru ndipo mudziwe mphamvu ya zinthu zazing'ono.

## ZIKOKA ZA UCHIMO ZILI PAKATI PATHU

Zintchito za thupi-dama, chigololo, utchisi, kupembedza



*Ngati munthu ali m'thupi lanyamali,  
adzayesedwa ndi  
mphamvu ya chikoka.*

*(Zapitirira pa tsamba 6)*

(Kuchokera pa tsamba 5)

mafano, ufiti, masiliro, chidakwa ndi zina zotere (Agalatiya 5:19-21)—zadzaza pa dziko lino. Izo zalowa mu nyimbo, kupembedza mafano, masewero ndi zina zotere. Mwana wa Mulungu sangalolere dala zinthu zoipa kuti zimukope osakolola zinthu zoipa kuuzimu. Malemba amatiphunzitsa kuti “mayanjano oipa aipsa makhalidwe okoma” (1 Akorinto 15:33). Ngati munthu akhala mgulu la anthu osapembedza, pakupita kwa nthawi, uzimu wake udzafooka ndipo chiyero chake chidzaonongedwa. Chenjezo likuperedwa kuti tisakhale “omangidwa m'goli ndi osakhulupirira” (2 Akorinto 6:14). Tiyenera kusamalitsa pamene tikusankha anzanu makamaka abwenzi omanga nawo banja.

#### **TIKANE CHISAPEMBEDZO**

Malemba amatilangiza kuti tikanizikiretu komanso kudzialikitsa ku chikoka chilichonse cha uchimo. “Usalowe m'mayendedwe ochimwa...Pewapo, osapitamwo; patukapo, nupitirire” (Miyambo 4:14-15). Mutsutsane nazo ntchito za mdima (Aefeso 5:11). Anthu ambiri amayesetsa kudzilungamitsa pa zinthu zimene sizili zoyera. Mwana wa Mulungu amene ayenera kukhala wokhulupirika mpaka pamapeto ndiye mkhristu uyo amene aima njii! motsutsana ndi zikoka zonse zosalungama komanso amene sapereka mpata kwa mdierekezi (Aefeso 4:27). Pamene munthu atalikirana nazo zikoka zoipa, izo sizikhala ndi mphamvu pa thupi lake. “Koma thawa zilakolako za unyamata, nutsate chilungamo, chikhulupiriro, chikondi, mtendere, pamodzi ndi iwo akuitana pa Ambuye ndi mitima yoyera” (2 Timoteo 2:22).

#### **TCHINJIRIZANI MAGANIZO NDI MTIMA**

Tchinjirizani maganizo anu ndi mtima wanu ku mphamvu ya uchimo ndipo musalolere zinthu izo zimene zingabweretse

kusangulama. “Chinjiriza mtima wako koposa zonse uzisunga; pakuti magwero a moyo atulukamo.” (Miyambo 4:23). Monga Davide anachitira, “Sindidzaike chinthu choipa pamaso panga...” (Masalmo 101:3). Mupatulule moyo wanu komanso nyumba yanu monga kachisi oyenera wa Mzimu Woyera. Ngati pali china chake chimene chili ndi chikoka choipa kuuzimu,



chisiyeni, ngakhale kutakhala kuti Akhristu ena akuchita zomwezo. “Koma ngati diso lako lamanja likulakwitsa iwe, ulikolowole, nuliitaye...” (Mateyu 5:29-30). Nkhani sikhala ya uchimo nthawi zonse. Ganizirani mphamvu ya chikoka. Monga Paulo ananena, “Zinthu zonse ziloledwa kwa ine; koma si zonse zipindula. Zinthu zonse ziloledwa kwa ine, koma sindidzalamulidwa nacho chimodzi.” (1 Akorinto 6:12).

#### **ZIKOKA ZABWINO**

Mmalo mokhala pa malo oipa amene ali ndi chikoka cha zinthu zadziko, titsate chiyero (Ahebri 12:13-15) komanso zinthu zonse zimene zimamangirira ndi kupe-reka chikoka chabwino. Mukhazikike ndi kukhala okhulupirika pa chiyanjano chanu ndi anthu a

*Mwana wa Mulungu ...aime njii motsutsana  
ndi zikoka zonse zosalungama  
ndipo asapereke mpata kwa mdierekezi.*

Mulungu (Ahebri 10:24-25). Mudzaze moyo wanu ndi zochitika komanso mautumiki amene amalimbikitsa kukula muuzimu. Musinthidwe ndi anthu oyera mtima koma makamaka ndi Mau a Mulungu. “Ndinawabisa mau anu mumtima mwanga, kuti ndisalakwire Inu” (Salmo 119:11).

#### **CHISANKHO NDI CHANU**

Pali mphamvu zazikulu zimene zimakhala ndi chikoka pa mkhristu wina aliyense, koma mwana wa Mulungu aliyense ali ndi chisankho pa za zimene angazilole pa moyo wake. Musankhe zikoka zabwino ndi zachiyero. “Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansu pano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire chimene chili chifuno cha Mulungu, chabwino, ndi chokondweretsa, ndi changwiwo” (Aroma 12:2).

-mws

# Muyeso wa Baibulo pa za Mafilimu ndi TV

Muyeso wa Baibulo pa zoonera mafilimu komanso TV wakutidwa m' mau amodzi basi: chiyero. Kukhala woyera ndiko kuyeretsedwa, kupatulidwa, wolungama, osadetsedwa, wapaderadera ndi kuchita mosasemphanitsa. Malemba amatiphunzitsa kuti “Ilemekezani Mulungu m'thupi lanu, ndi mzimu wanu zimene zili zake za Mulungu” (I Akorinto 6:20). “Pakuti Mulungu sanaitana ife titsate chidetso, koma chiyeretso” (I Atesalonika 4:7). Popanda chiyero, “palibe mmodzi adzaona Ambuye” (Ahebri 12:14). Munthu ayenera kuganizira mphamvu ndi chikoka zimene zimapezeka mu mafilimu ndi ma TV ndiponso aziyese molingana ndi malemba amene ali pamwambapa. Ife pokhala ana a Mulungu, malemba akuti “chitani zonse ku ulemerero wa Mulungu” (I Akorinto 10:31).

Palibe uchimo uliwonse mu nzeru zopangira makanema kapena mu zipangizo kapenanso mu kanemayo. Nkhani yagona pa zimene tasankha kuti tionere komanso zotsatira zake patapita nthawi. Mafilimu ndi ma TV masiku ano kwambiri akuonetsetsa zinthu zonyansa ndi zolaula. Agalatiya 5:19-21 akutionetsa ntchito za thupi kuti ndizo: “dama, chodetsa, kukhumba zonyansa, kupembedza mafano, nyanga, madano, ndeu, kaduka, zopsa mtima, zotetana, magawano, mipatuko, njiru, kuledzera, mchezo...Iwo akuchitachita zotere sadzalowa Ufumu wa Mulungu.” Mafilimu ambiri amaonetsetsa zinthu izi zimene zanenedwa ngati ntchito za thupi. Tsono nanga ndi chifukwa chiyani mwana wa Mulungu amene akufuna kukhala moyo wachiyero angalole judzadzitsa mtima wake ndi maganizo ake ndi zinthu zimene zili zodziwikiratu kuti ndi zachikunja?

Nyumba ya munthu woyera mtima idzikhala ngati kothawirako ndiponso kopumulirako ku zonyansa za dziko lino. Pali zinthu zambiri zathupi zimene zili ndi mphamvu komanso chikoka pa dziko lino ngakhale sizichitikira kunyumba. Mafilimu komanso zoonetsa pa TV zikhoza kukhala zokoma ku thupi, koma taitanidwa kuti tikapachike thupi lathu ndi zikhumbitso komanso zilakolako zake ndipo tiyende mwa Mzimu. Malemba akulangiza thupi lonse la Khristu za zimene tiyenera kuganiza: “Chotsalira, abale, zinthu zili-

zonse zoonera, zilizonse zolemekezeka, zilizonse zolungama, zilizonse zoyera, zilizonse zokongola, zilizonse zimveka zokoma; ngati kuli chokoma mtima china, kapena chitamando china, zilingirireni izi” (Afilipi 4:8).

Zinthu izi zimakhala zodziwika pamene zayesedwa mu mitima yoyera ndi Mau a Mulungu. Kodi munthu amachimwa chifukwa chakuti waonera filimu basi? Ayi ndithu, koma pamene tiganizira za mphamvu ndi chikoka chosalungama chimene chimakhala kuseli kwa mafilimu ndi ma pulogalamu a pa TV ambiri, zingakhale zabwino kudziletsa kuti potero tisakopeke. Mdaniyo wagwiritsa ntchito chikoka chachikulu chimene chimapezeka mu ma filimu ndi ma pulogalamu a pa TV ngati chida chachikulu chowonongera

uzimu ndi khalidwe labwino ku mibadwo yambiri. Utolankhani umene nawonso wadzaza ndi uchimo uli ndi kampeni kumphasa ndipo sizichita kutengera kufufuza mozama kuti tizindikire zolinga zauchimo komanso zikhaliidwe zina zimene zikulimbikitsidwa kwambiri.

Zotsatira za kalemba ndi kafukufuku zikuonetsetsa ndi kutsimikiza kambirimbiri kuti kuonera TV kumaononga ana. Gawo lalikulu la mafilimu ndi ma pulogalamu a pa TV amaonetsetsa zikhaliidwe zachikunja. Zoterezi zimaononga ana ndipo zima-

pangitsa kuti akhale ndi moyo wauchigawenga, okonda zandeu, kumwa mankhwala osokoneza bongo, kunenepa mopyolera muyeso, kuchita zachiwerewere, kusadzikhulupirira kuti angathe kuchita zinthu, komanso kusachita bwino pa maphunziro. Ngati mwana akungokhalira kuonera TV, mpata wakuti akhoza kutsanzira zimene akuonerazo ndi waukulu. Mafilimu ambiri amapereka chinthunzi cha zinthu zenizeni pamaso koma kuseri kwake zili zabodza komanso saonetsetsa zotsatira zake za chikhaliidwe chauchimo. Zinthu izi zimabzala mbeu yolakwika mwa ana ndipo ziwawimbikitsa iwo kuti adziona ngati uchimo ndi wosangalatsa komanso wovomerezeka.

Aliyense, koma makamaka ana ndi achinyamata amate-ngeka ndi zimene akuona komanso kuonera. Ndikukumbikira kuti ndimalankhula ndi mnyamata wina ku msonkhano

(Zapitirira pa tsamba 8)



**Tsono nanga ndi chifukwa chiyani mwana wa Mulungu amene akufuna kukhala ndi moyo wachiyero angalole judzadzitsa mtima wake ndi maganizo ake ndi zinthu zimene zili zodziwikiratu kuti ndi zachikunja?**

(Kuchokera pa tsamba 7)

wina wa mpingo. Iye anali wodabwa kumva kuti ndinakwera ndege popita kumeneko. Iye anandiuza kuti, “Ine zimenezo sindingayerekeze.” Iye amaopa kukwera ndege chifukwa cha filimu ina yochititsa mantha imene iye anaonera imene mu ndege munali njoka zambiri. Kenaka anandiuza kuti sanga kwere sitima ya pa mtunda chifukwa cha zinazake zimene ana ziona. Tiyenera kusamalitsa ndi kuzindikira mphamvu yaikulu imene ili mu mafilimu.

Anthu ena amanena kuti, “Ine ndimangoonera mafilimu ndi ma pulogalamu abwino okhaokha.” Izi zikhoza kukhaladi zoono, komano tikawafufuza, kodi ndi mafilimu a chiyerodi? Moti palibe mau ena kapena zoonetsa zina zosakhala bwino? Kodi siziyamwa uzimu wanu ndi kukudyerani nthawi? Munthu akayamba kuonera mafilimu, mwa iye njala ndi chikhumbokhumbo chomaone-raonera chimanka chikulirakulira. Kanthu kamene kanayamba ngati kabwino kakhoza kusanduka ‘chizolowezi’ ndipo moyo wa munthuyo umakhala mu zimene akuonerazo.

Anthu abwino ambiri amayamba kuonera mafilimu amene amaona kuti ndi abwino, komabe nkupita ka nthawi, samvetseranso ku liu la kayaziya la Mzimu, ndipo amaonera zambiri zachikunja. Kumakhala kovuta kwa iwo kusiyantsa ndikufika poleka kuonera. Zimatengera chifundo cha Mulungu kuti iwo adzuke ku tulo timeneti nazindikira zimene akhala akuzilola pamoyo wao. TV imagwiritsidwa ntchito kwambiri ngati chida cha msangulutso, komano mmenemo mumakhala zilakolako za thupi, zilakolako za maso ndi matamandidwe a moyo. Zinthu izi sizichokera kwa Mulungu ndipo tiyenera kuzikana pa moyo wathu. Mauthenga ambiri amene amaonetsedwa pa TV amakhala pa nthawi ya pakati pa ma pulogalamu ofunikira monga nkhani ndi enanso abwino. Mauthengawa amakhala ochititsa manyazi kwa mwana wa Mulungu. Izi zimakhala ndi chikoka ndipo pakapita nthawi munthu akungoonerabe mauthengawo, kenaka saona cholakwika ndipo mzimu wake sumva kutsutsika pakakhala kuti pali zachikunja. Kenaka amayamba kuchepetsa mfundo za choonadi komanso chiyero cha mumtima. Chikoka ichi cha zinthu zachikunja zakhala ngati nyambo komanso msampha

kwa akhristu ambiri. Chenjerani!

Mafilimu amadya nthawi yochulukira imene Mulungu amafuna akadayanjana nafe pomutumikira komanso pomupembedza. Kuonera mafilimu ndi TV komanso kumapangitsa kutopa komanso thupi kufooka. Zimapangitsa kuti kaganizidwe kathu kakhale kocheperapo. Kumakhala kovuta kuti munthu apemphere ndi kuwerenga mau. Zimakhala zovuta kwambiri kuti munthu akhale tcheru pamene ali mkalasi kapena mtchali.



**Pamene munthu wayamba kuonera mafilimu, kawirikawiri izi zimalimbikitsa chikhumbokhumbo ndi chilakolako chofuna kumangoonerabe.**

TV komanso mafilimu akhala akugwiritsidwa ntchito padziko lonse pofuna kufalitsa uchimo. Ineyo ndakhala ndikuziona izi ziku-chitika m’ madera amene chitukuko sichinafike kwenikweni. Ndaona ‘chikhalidwe chauchimo cha kwa azungu’ chikufala kudzera mkuonera mafilimu ndi zina zosangalatsa moyo. Akhristu a m’ maiko amenewa amazindikira chikoka choipa ndi champhamvu chimene chimbwera ndi zinthu zimene anthu amaonera pa TV. Zinthu zochotsa ulemu zimaonetsedwa komanso kulemekezedwa ndipo anthu amayesera kutsatira zitsanzo za zinthu izi zooneka ngati zosangalatsa ndi zokoma. Mulungu watiyitana kuti tikhale moyo wachiyero

ndipo tiyenera kudziletsa ku zinthu zauchimo zimene zikuchitika mnthawi yathu ino.

Kachiwirinso, kodi muyeso wa baibulo pa kuonera mafilimu ndi TV ndi wotani? Mudziweruze nokha pamaso pa Mulungu ndi mau ake. Chiyero ndiye chofunikira. Nkhani yake si chimene chikugwiritsidwa ntchito pofuna nkuonera (kaya ndi filimu, video, DVD, TV komanso intaneti) koma chikoka cha zinthu zimene mkuonera. Samalani ndipo chitani mochenjera.

Ana a Mulungu akuyitanidwa kuti akhale zitsanzo komanso kuwala kwa dziko lapansi. Ichi chokha chiyenera kutipangitsa kuti tidzichenjera ndi kukhala osamalitsa pa zinthu zimene tingazilole kuti zilowe m’ moyo wathu. Atsogoleri ndi abusa akuyenera kukhala zitsanzo za kukhala mmoyo wachiyero ndi waumulungu.

Mfumu Davide ananena mwachimvekere ndi moona mtima pa Masalmo 101:3 kuti: “Sindidzaika chinthu choipa pamaso panganga; chochita iwo akupatuka padera chindiipira; sichidzandimamatira.”

-mws

# Mafunso ndi Mayankho

**Funso:** Kodi kugwiritsa ntchito intaneti kutenge gawo lotani pa moyo wa Mkhristu?

**Yankho:** Pali mafunso ambiri amene afunsidwa ngati kuli koyenera kuti woyera mtima agwiritse ntchito intaneti kapena ayi. Kodi kugwiritsa ntchito intaneti kutenge gawo lotani pa moyo wa Mkhristu. Kodi kusiyana kwa intaneti ndi TV ndi kotani? Kodi munthu akaonera chimodzi nkusiya chinzake walakwa?

Nkofunikira kuzindikira kusiyana kwake kwa TV ndi intaneti. Cholinga chenicheni chachikulu cha TV ndicho kusangalatsa anthu, kaya ndi mafilimu kapena masewera. Nkhaninso zimaonetsedwa pa TV komabe tione kuti kwakukulu chimaoonetsedwa ndi chiyani pa TV.

Intaneti ili ngati kangaude wa nkhani zosiyanasiyana zimene zalukana kuchochera ku mbali iliyonse ya dziko lapansi. Intaneti imagwiritsidwa ntchito m'maofesi ndi ntchito zina, pofuna kulumikizana ndi anthu ena komanso pa za kafukufuku ndi zina zotere. Intaneti ndi chida chothandiza kwambiri, komanso ikhoza kugwiritsidwa ntchito pa zinthu zoipa. Masiku ano pa intaneti pamapezekanso mafilimu ndi zina zambiri zime ne zimaonetsedwa pa TV. Mwachidule, kudzera pa intaneti, anthu amachita zinthu zoopsa zauchimo kuposanso mwina poonera TV. Komabe pali kusiyana. Pali mwayi waukulu wakuti munthu akhoza kudziletsa pa intaneti kusiyana ndi pa TV pamene omwe amakonza zoti muonere ndi eni ake a zoonetsedwazo. Komabe, uchimo waukulu umachitika

pamene anthu ali pa intaneti. Masiku ano anthu sapitanso ku malo obisika kukachita uchimo ndi kukwaniritsa zikhumbitso zawo. Iwo amatha kukhala pa intaneti mkati mwa mnyumba zawo. Choncho, intaneti ikhoza kukhala chida chofunikira komanso chida choopsa kwambiri.

Chiphunzitso cha chiyero tiyenera kuchigwiritsa mosanyengerera pamene tikuona za intaneti ngati chida. Ngati chingakhale chida cha chisangalalo basi, nchachidziwikire kuti anthu ambiri ayamba kusalabadira mfundo zawo za chiyero. Intaneti yasaduka ngati njira yozembera mavuto ndi nyengo zosautsa. Mmalogona, anthu



amakhala nthawi yochuluka mpaka usiku ali pa intaneti. Ambiri amakhala m'moyo waokha osafuna kukhala pakati pa anzawo ndi achibale awo. Mmalogona amamva bwino kukhala pa intaneti chifukwa ndi zimene dzikoli lalenga masiku ano. Nchifukwa chake tiyenera kusamala kwambiri.

Intaneti ili ngati mfuti yodzaza ndi zipolopolo. Suyenera kuyiseweretsa koma kuyigwiritsa ntchito mosamala komanso kuzindikira kuti ndi chida choopsa ngakhale chili chofunikira. Pali anthu ena amene sayenera kukhala nayo kapena kugwiritsa ntchito mfuti. Izi zili chimodzimodzi ndi intaneti. Pali anthu ena amene sayenera nkomwe kuledwa kugwiritsa ntchito intaneti ngati njira yowatchinjirizira iwo ndi kuwateteza malingana ndi chifooko chawo.

Intaneti itagwiritsidwa ntchito moyenera, ingathe kuthandiza pa zinthu zambiri. Iyenera kukhala yosadetsedwa. Nthawi zambiri imalowa mmalo mwa nthawi yowerenga mau a Mulungu ndi kupemphera kapenanso chochitika pofuna kupititsa nthawi. Anthu amategekka ndi kugwiritsa ntchito intaneti komanso chidwi chawo chofunafuna mbiri ya zinthu chimachulukika. Choncho kudziletsa ndi kofunikira ndithu ndipo ndi koyenera kuunikanso kagwiritsidwe ntchito ka intaneti kunyumba.

Zinthu ngati fesibuku zikhoza kugwiritsidwa ntchito pa zinthu zauzimu kapekana kulumikizana ndi anzathu. Koma zikagwiritsidwa ntchito molakwika zikhoza kukhala zoopsa kwambiri. Makomo komanso mabanja ambiri awonongeka komanso kupasuka chifukwa cha kucheza pa fesibuku kumene kunayamba ngati zabwinobwino. Makoma ndi maulemu pakati pa achinyamata ndi akulu amene Ambuye akadakonda kuti asungidwe agwetsedwa chifukwa cha zinthu ngati fesibuku.

Monga momwe mfuti yodzaza ndi zipolopolo

imayenera kusungidwa pamalo abwino, nchimodzimodzinso intaneti imene imapezeka mnyumba za anthu. Ana akuyenera kuyang'aniridwa bwino ngati akugwiritsa ntchito intaneti pa za sukulu ndi pochita kafukufuku. Kungakhale bwino kutseka zinthu zina pofuna kuwateteza anawo ku mayesero.

Tili mu nyengo imene zambiri zimayendera makina ndipo intaneti yakhala chida chofunikira kwambiri. Tiyeneranso kuzindikira kuopsa kwake kwake intaneti. Moyo wanu ndi wofunikira koposa kena kalikonse. Zisankho zanu zionetsere chimenechi ndipo chiyero, kuleza mtima ndi kusamalitsa zionetsedwe nthawi iliyonse imene mukugwiritsa ntchito intaneti.

-mws



KODI MUKUDZIWA?

## Mayimbidwe ali ndi chikoka chachikulu pa anthu.

Kuyimba kumawulula nyengo ndi zikhalidwe zathu ndipo kuli ndi mphamvu yopangitsa anthu kuti asangalale, amve chisoni, akwiye ndi zina. Mayimbidwe osiyanasiyana okhala ndi mau komanso chamba chawochawo amakhala ndi chikoka cha mmene munthu angalimvere ndi kulionera dzikoli. Anthu ambiri pofuna kutonthozedwa ndi kusangulutsidwa amamvera kapena kuyimba nyimbo. Mayimbidwe akhoza kukhala njira yopembedzera Mulungu komanso ngati njira yofuna kuyiwalira mavuto a moyo uno.



**Kodi mayimbidwe amagwira ntchito pa moyo wanu?** Kodi ndi zabwino, zolungama ndi zopatulika? Kodi zikukwaniritsa chosowa chimene Mulungu amafuna kuchikwaniritsa?



Mau a pa  
Nyengo Yake

## Nkhondo Siyanu

### Kuti Mutipeze

The Gospel Truth  
P.O. Box 2042  
Nixa, MO 65714  
USA  
Email:  
editor@thegospeltruth.org

CHIYERO KWA AMBUYE

*Atero nanu Yehova, Musaope musatenge nkhawa chifukwa cha aunyanji ambiri awa; pakuti nkhondoyi si yanu, koma ya Mulungu. —2 Mbiri 20:15b*

Yehosafati analandira uthenga wakuti gulu la ankhondo lalikulu likubwera kudzachita naye nkhondo. Iye anayang'ana kwa Yehova nati “ndipo sitidziwa ngati tidzalani, koma maso athu ali kwa Inu.” (12).

Mdaniyo akugwiritsa ntchito china chilichonse kuyesetsa kuti akhumudwitse anthu a Mulungu. Mdierekezi akupenyetsa kwa atumiki oona, odzazidwa ndi Mzimu Woyera amene akudzipereka kwathunthu chifukwa cha Uthenga Wabwino. Pali zinthu zambiri zimene zimachitika zimene zimapangitsa kuti nkhondo zimene timakumana nazo zioneke zolimba mphamvu ndi zazikulu kwa ifeyo. Zimatichitira ubwino pamene tizindikira ndi kuvomereza chosowa chathu, monga mmene anachitira Yehosafati, ndipo nkuika maso athu pa Mpulumutsi.



Nkhani yokondweretsa imene Mzimu wa Mulungu anapereka kwa Yehosafati ndi yomweyonso imene Ambuye akuwuzana anthu ake lero lino. “Musaope; pakuti nkhondoyi si yanu, koma ya Mulungu.” Mtendere waukulu umapezeka pamene tizindikira kuti Mulungu ndi amene akulamulira ndipo ife sityenera kukhala ndi mayankho onse kapena kuthekera kogonjetsa gulu lalikulu sikuli mu mphamvu zathu.

Yehosafati anauzidwa kuti “chilimikani, imani, nimupenye chipulumutso cha Yehova” (17). Tiyeni tisasunthike ndipo tikhazikike pa chitsimikizo chakuti Ambuye asamalira iwo amene ali ake.

-mws